EXAMINATION NUMBER: ______________________

# ZOMBA RURAL DISTRICT EXAMINATION BOARD

## 2024 PRIMARY SCHOOL LEAVING CERTIFICATE MOCK EXAMINATION

# CHICHEWA

**(Malikisi 100)**

**Subject Number:**

**Tsiku: 4th** April, 2024

**Nthawi:** 2hrs 15 mins
13: 00 - 15: 15 pm

**DZINA LA OPHUNZIRA:** ____________________________________________
**(Surname first)**
**DZINA LA SCHOOL:** ______________________________ **ZONE** ____________

## Instructions:

1. **Onetsetsani kuti pepala ili lili ndi masamba asanu ndi anayi**
2. Pepala ili lili ndi magawo anayi: **Gawo A, B, C** ndi **D.**
3. Lembani **dzina** lanu ndi **dzina la sukulu** yanu pamwamba pa tsamba lino.
4. Lembani Chimangirizo kapena Kalata mu **Gawo A** ndipo muyankhe mafunso onse mu **Gawo B, C** ndi **D**.
5. Lembani yankho lanu mu **Gawo A** pa mipata yomwe yapatsidwa.
6. Yankhani mafunso a mu **Gawo B** ndi **C** m'mipata yomwe yaperekedwa pasni pa funso lililonse.
7. Yankhani mafunso a mu **Gawo D** pozunguliza lembo lokhoza pa funso lililonse.
8. Muchitebulo chili pa mwambachi onetsani funso lililonse lomwe mwayankha pochonga mubokosi lomwe lili kutsogolo kwake.
9. Perekani kwa oyang'anira kulemba mayeso **(invigilator)** pepala lonseli nthawi ikakwana.

| **Question Number** | **Tick if answered** | **Do not write in these columns** | |
|---|---|---|---|
| **1** | | | |
| **2** | | | |
| **3** | | | |
| **4** | | | |
| **5** | | | |
| **6 – 45** | | | |
| | | | |



**© DIP 2024**

EXAMINATION NUMBER: ______________________

**Gawo A** (malikisi 30)

Yankhani funso limodzi lokha mwa mafunso awiri ali m'munsiwa. Sankhani mutu wa Chimangirizo kapena wa Kalata. Mawu a Chimangirizo chanu kapena Kalata yanu asachepere **100** komanso asabzole **150**.

**1.** Lembani Chimangirizo pa mutu uwu: **MADZI OSEFUKIRA**

Mwa zina tsatani izi polemba;

**Ndime yoyamba**

- Tsiku ndi nthawi yomwe madzi adasefukira
- Komwe mudali panthawiyo
- Dela lomwe lidakhudzidwa ndi madzi osefukira

**Ndime yachiwiri**

- Zinthu zomwe zidawonongeka ndi madziwo
- Momwe dela lanu lidakhudzidwira ndi madzi osefukirawo.

**Ndime yachitatu**

- Chithandizo chomwe mudalandira potsatira kusefukira kwa madziwo
- Zomwe mukuchita pofuna kupewa kusefukira kwa madziwo

**KAPENA**

**2.** Lembani kalata kwa mzanu yomufotokozera mmene mwakonzekera mayeso a boma omwe mulembe chaka chino

Mwa zina tsatani izi polemba:

**Ndime yoyamba**

- Cholinga cha kalata
- Mwezi wodzalemba mayeso
- Zomwe mukuchita pokonzekera mayesowo

**Ndime yachiwiri**

- Thandizo lomwe mukupeza pokonzekera mayesowo
- Chiyembekezo chanu pamayesowo

**Ndime yachitatu**

- Momwe mudzasangalalire mukadzapambana mayesowo


© DIP 2024

 **© DIP 2024**

## GAWO B: KUMVETSA NKHANI (malikisi 20)

**3.** Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kwambiri kenako yankhani mafunso otsatirawo.

Atadzidabwa Tadala yemwe adali mwana wa chisamba banja la a Gama, adali ndi anzake omwe amacheza nawo. Pakuti ena mwa anzakewo adali maunthu sadadziwe kalikonse. Pagululi ena adali anamwali omwe atamva zimene Tadala amanena adangotsinzinirana. Iwo adachita izi podziwa kuti bongololo sadzolera mafuta pa gulu. Makamaka sadafune kulawulira amene anali asanagwe m'dothi. Atsikanawa adadziwa kuti tsopano Tadala ndi namwali mnzawo. Pa nthawiyi atsikanawa ankachokera ku madimba atadendekera nsengwa za ndiwo zoti akadyere nkhomaliro.

Mwa atsikanawa maunthu adali Ulemu, Zione ndi Mandaaliza. Enawo adali; Alefa ndi Omega. Onse adali atsikana a m'mudzi mwa Ndalawira. Mudziwu umatchuka ndi gule wa chimtali. Atafika kumudzi anamwali aja adadziwitsa mayi ake a Tadala. Nthawi yomweyo amakewa adatengera nkhaniyo kwa namkungwi. Atamva izi namkungwi sadafune kuchedwa. Iye adawuza ntchemberegandule za pa mudzipo. Iwo adatsinana khutu ndipo adagwirizana zokhala naye pansi mtsikanayo. Kutacha adamuyitana Tadala kuti akakumane naye m'kanyumba komata.

Namkungwi Zukira adali wotchuka m'mudzimo polangiza atsikana othyola bano. Aliyense amadziwa kuti munthu wolangizidwa ndi a Zukira samachititsa manyazi Asanayambe kulangiza namkungwiyo adali atakanena kale kwa mfumu a M'bebe kuti pamudzi pawo padali mlango wa namwali kuwopa kudula mfumu. Zokonzekera zonse zitatha, ntchembere zidayamba kulangiza Tadala uja. Zina mwa zomwe adamulangiza ndi zoti kuyambira tsiku limenelo asamafikire kukhala akalowa m'nyumba ya makolo. Masiku ngati amenewa asathire mchere m'ndiwo. Azikhala wa ukhondo ndipo akamadutsana ndi munthu wamkulu amayenera ku gwada kwinaku akuomba m'manja ali zyoli. Kamba ka malangizowa Tadala adakula ndi mwambo.

**Tsopano yankhani mafunso otsatirawa pa mizere ili pansi pa funso lililonse.**

**a.** Kodi Tadala adali yani? **(malikisi 1)**

______________________________________________

______________________________________________

**b.** Tchulani maunthu awiri omwe atchulidwa mu nkhaniyi **(malikisi 2)**

______________________________________________

______________________________________________

**c.** N'chifukwa chiyani anamwali aja sananene chirichonse pa zomwe zidamuchitikira Tadala mu njira **(malikisi 2)**

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

**d.** Kodi atsikana adatenganji pa mitu yawo? **(malikisi 1)**

______________________________________________

______________________________________________

**e.** N'chifukwa chiyani mudzi wa M'bebe udali wodziwika? **(malikisi 1)**

______________________________________________

______________________________________________

**f.** Ndani adakadziwitsa amfumu nkhani ya Tadala? **(malikisi 1)**


© DIP 2024

---

**g.** Perekani matanthauzo a mau awa?

(i) Asanagwe m'dothi

______________________________ **(malikisi 1)**

(ii) Ntchemberegandule

______________________________ **(malikisi 1)**

**h.** Kodi Tadala ndi anzake amachokera kuti pamene ankadzidabwa? **(malikisi 1)**

______________________________

______________________________

**i.** Kodi kufunika kouza amfumu nkhani zokhuza Tadala kudali kotani? **(malikisi 2)**

______________________________

______________________________

**j.** Tchulani namkungwi wotchuka polangiza atsikana othyola bano m'mudzi wa M'bebe **(malikisi 1)**

______________________________

**k.** Perekani mawu otsutsana m'matanthauzo ndi mawu awa kuchokera m'nkhaniyi

(i) Weramuka: ______________________________ **(malikisi 1)**

(ii) Bunthu: ______________________________ **(malikisi 1)**

**l.** Fotokozani zinthu ziwiri zomwe adamulangiza Tadala

(i) ______________________________

**(ii)** ______________________________ **(malikisi 2)**

**m.** Perekani mutu wa nkhaniyi

______________________________ **(malikisi 2)**

**GAWO C** (malikisi 10)

**Yankhani mafunso onse awiri m'gawoli**

**4.** Werengani kankhanika ndipo muyankhe mafunso otsatirawo

' Tsopano ndimulore kuti aloze yekha yemwe adampatsa chinjacho. Akatero timtengera pena.'

**Mafunso**

**a.** i. Ndi malonje anji amenewa? **(malikisi 1)**

______________________________

ii. Kodi mawu oti 'chinjacho' atanthauzanji? **(malikisi 1)**

______________________________

iii. Kodi angayankhule mawu amenewa ndindani? **(malikisi 1)**

______________________________

**b.** Kodi munthu oyenda pansi ayenera kuyenda mbali iti ya msewu? **(malikisi 1)**


**© DIP 2024**

______________________________________________________________

**c.** Tchulani mchitidwe umodzi omwe umalepheretsa atsikana kumaliza maphunziro awo?**(malikisi 1)**

______________________________________________________________

**5. Kupanga ziganizo**

Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa:

**a.** ngati **(malikisi 1)**

______________________________________________________________

**b.** njenjemera **(malikisi 1)**

______________________________________________________________

**c.** ndi **(malikisi 1)**

______________________________________________________________

**d.** pikitipikiti **(malikisi 1)**

______________________________________________________________

**e.** waulesi **(malikisi 1)**

______________________________________________________________

**Gawo D** (malikisi 40)

Zungulizani lembo lokhoza **(A, B, C** kapena **D)** m'mafunso otsatirawa.

**Mafunso 6 mpaka 10:** Sankhani mitundu ya mawu amene atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi:

**6.** Mbewa zonse zija zalowa pa dzenje la njoka.
- A. muonjezi C. mlowammalo
- B. mperekezi D. mlumikizi

**7.** Mariya sindidafune kukhala naye chifukwa masiku ano akutchuka ndi utsinzinantole.
- A. muonjezi C. mfotokozi
- B. mlowa mmalo D. mlumikizi

**8.** Aliyense wapita kwao.
- A. Mlowa mmalo C. dzina
- B. mfotokozi D. muonjezi

**9.** Munthu yemwe abwere ndi wamtali.
- A. Mlowa mmalo C. mfotokozi
- B. dzina D. muonjezi

**10.** Amayi akanitsitsa kuti si mfiti.
- A. muonjezi C. mneni
- B. mfotokozi D. mperekezi

**Mafunso 11 mpaka 15:** Sankhani mawu omwe akusonyeza kuchuluka kwa mawu ali ndi mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi

**11.** Kuseli kwa nyumba yathu kuli njoka.
- A. njoka
- B. zinjoka
- C. manjoka
- D. anjoka

**12.** Khasu langa lasowa.
- A. makhasu
- B. zimakasu
- C. zimakhasu
- D. makasu

**13.** Mariya akufuna kudzakhala mphunzisi akatsiriza sukulu.
- A. maphunzitsi C. mphunzitsi
- B. aziphunzitsi D. aphunzitsi

**14.** Amayi andipatsa msoti umodzi wokha kuti ndikawete.

 **© DIP 2024**

A. msoti C. misoti
B. dzimsoti D. Zimisoti

**15.** kwathu kuli kamphaka
A. Zimphaka
B. Tiamphaka
C. Amphaka
D. Mphaka

**Mafunso 16 mpaka 20:** Sankhani mitundu ya misintho ya aneni omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.

**16.** Amayi amagonagona akachoka ku ntchito.
A. wochititsitsa
B. wotsutsa
C. wobwerezabwereza
D. wochitirana

**17.** Galu wagundidwa ndi galimoto.
A. wochitidwa
B. wochititsa
C. wochitirana
D. wom'chitira

**18.** Iwo aphetsa mwana uja.
A. wochititsitsa
B. wom'chitira
C. wochititsa
D. wochitidwa

**19.** Penyetsetsa kuti uwonetsetse bwino.
A. wochitirana
B. wom'chitira
C. wochititsa
D. wochititsitsa

**20.** Nduna yamangira nyumba agogo a m'mudzi
A. Wotsutsa
B. Wom'chitira
C. Wochitirana
D. wochitidwa

**Mafunso 21 mpaka 25:** Sankhani chiganizo chomwe chili ndi zizindikiro zoyenera za m'kalembedwe m'ziganizo zotsatirazi

**21.**
A. Kodi dzina lako ndiwe yani!
B. Kodi dzina lako ndiwe yani.
C. Kodi dzina lako ndiwe yani?
D. kodi dzina lako ndiwe yani?

**22.**
A. Chikondi amayenda, monyada.
B. Chikondi; amayenda monyada.
C. Chikondi amayenda; monyada.
D. Chikondi amayenda monyada.

**23.**
A. Kwathu kuli mitengo ya mango, papaya ndi masuku.
B. Kwathu, kuli mitengo ya mango, papaya ndi masuku.
C. Kwathu kuli mitengo ya mango, papaya, ndi masuku.
D. Kwathu kuli mitengo ya mango papaya ndi masuku

**24.**
A. Atate, adati "kusuta kumaononga moyo."
B. Atate adati, "kusuta kumaononga moyo."
C. "Atate, adati," kusuta kumaononga moyo.
D. Atate adati, "kusuta kumaononga moyo!"

**25.**
A. Ogo! Ndayiwala zinthu zanga.
B. Ogo, Ndayiwala zinthu zanga.
C. Ogo! ndayiwala zinthu zanga.
D. Ogo ndayiwala zinthu zanga.

**Mafunso 26 mpaka 30:** Sankhani mawu ofanana matanthauzo ndi omwe ali ndi mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

**26.** Mariya adakwatiwa ndi sizinantole
A. wogodomala C. wolongolola
B. wosakongola D. wakuba

**27.** Tinyade wandigulira nkafanzayera


© **DIP 2024**

A. wolekanitsa C. wopeneka
B. wa chifukwa D. wotukuka

**28.** Bambo Chisa adali wokhupuka.
A. wochenjera C. wozitukumula
B. wolemera D. wacholinga

**29.** Eni ake a nyumba iyo ndi phungu-satayanthenga
A. owumira C. adyera
B. atulo D. oyendayenda

**30.** Iwo adakwatira nyenyezi.
A. mzakazi C. njole
B. kalilore D. banja

**Mafunso 31 mpaka 35:** Sankhani mawu oyenera kutsirizira mikuluwiko yotsatirayi

**31.** Chisoni chidaphetsa _________________
A. nkhunda C. nkhwali
B. nkhuku D. nkhawena

**32.** Umanena chatsitsa _________ kuti njovu ithyoke m'nyanga.
A. dzaye C. bango
B. lalanje D. tsiku

**33.** _________ sadzolera mafuta pagulu.
A. Nyani C. Namwali
B. Bongololo D. Asakhwi

**34.** Njiwa sasosolera pa ____________________.
A. nyumba C. tchire
B. njira D. msampha

**35.** Ali dere n'kulinga ___________ naye.
A. utacheza C. utasamba
B. utavina D. utayenda

**Mafunso 36 mpaka 40:** Sankhani mitundu ya nthambi za chiganizo yomwe yatsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.

**36.** Mwana amene akudwala ndi wanga.
A. yoyima payokha
B. ya mfotokozi
C. ya muonjezi
D. ya dzina

**37.** Aphunzitsi adanena kuti ndidziwerenga
A. ya mfotokozi
B. yoyima payokha
C. ya dzina
D. ya muonjezi

**38.** Chuma wagona chifukwa wadwala.
A. ya muonjezi
B. ya mfotokozi
C. yoyima payokha
D. ya dzina

**39.** Sindikudziwa chimene akufuna
A. ya mfotokozi
B. yoyima payokha
C. ya muonjezi
D. ya dzina

**40.** Ngakhale ubwere sindikupatsa.
A. ya dzina
B. ya muonjezi
C. yoyima payokha
D. ya mfotokozi

**Mafunso 41 mpaka 45:** Sankhani mitundu ya ziganizo zotsatirazi.

**41.** Zione wabwera koma akudwala
A. chiganizo chopanda nthambi
B. chiganizo cha nthambi
C. chiganizo cha ziganizo zingapo
D. chiganizo choyima pawokha

**42.** Sizoona kuti agogo abwere mawa
A. chiganizo chosaima pachokha
B. chiganizo chanthambi
C. chiganizo cha ziganizo zingapo
D. chiganizo chopanda nthambi


© **DIP 2024**

**43.** Manase abwera mawa
- A. Chiganizo chopanda nthambi
- B. Chiganizo chosaima pachokha
- C. Chiganizo cha nthambi
- D. Chiganizo cha ziganizo zingapo

**Mafunso 44 mpaka 45:** Sankhani mitundu ya nthawi za aneni omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

**44.** Iye amakhala ku Mzuzu.
- A. yam'tsogolo
- B. yatsopano
- C. yatsopano yopitilira
- D. yam'tsogolo yopitilira

**45.** Ndalemba kalata yopita kwa mayi ako
- A. yatsopano yathayi
- B. yatsopano
- C. yatsopano yopitilira
- D. yatsopano ya mtsogolo

Mafunso athera apa



**© DIP 2024**